NAMBALA YA MAYESO .: ____________________________

# CHIMUTU CLUSTER EXAMINATION BOARD

**2024 END OF TERM TWO STANDARDIZED EXAMINATION FOR STANDARD 8**

## CHICHEWA

**(100 Malikisi)**

**Subject Number: P032**

**Nthawi: 2hr 15min**
**1:00 – 3:15pm**

**Tsiku: _____/ ______/ 2024**

**DZINA LA OPHUNZIRA:** ____________________________________________________________
**(*Kuyamba ndi bambo)***
**DZINA LA SUKULU:** ____________________________________________________________

**Malangizo**

1. Pepalaili lili ndi magawo **anayi** Gawo A, B , C ndi D
2. Lembani **dzina lanu** ndi **dzina la sukulu** yanu pamwamba pa tsamba lino.
3. Lembani chimangirizo kapena kalata mu gawo A ndipo muyankhe mafunso onse mu gawo B, C ndi D
4. Yankhani mafunso a mu gawo B ndi C m'mipata yomwe yaperekedwa pansi pa funso lililonse
5. Yankhani mafunso a mu gawo D pozungulirza lembo lokhoza pafunso lililonse
6. Muchitebulo chili pamwambachi onetsetsani funso lililonse lomwe mwayankha **pochonga** mubokosi lomwe lili kutsogolo kwake.
7. Perekani kwa **oyang'anira mayeso** pepala lonseli nthawi ikakwana

| Mafunso | Chongani funso lomwe mwayankha | Muno musalembemo kanthu | |
|---|---|---|---|
| 1 | | | |
| 2 | | | |
| 3 | | | |
| 4 | | | |
| 5 | | | |
| 6 – 10 | | | |
| 11 – 15 | | | |
| 16 – 20 | | | |
| 21 – 25 | | | |
| 26 – 30 | | | |
| 31 – 35 | | | |
| 36 – 40 | | | |
| 41 – 45 | | | |
| | | | |

NAMBALA YA MAYESO .: ____________________________

## GAWO A (MALIKISI 30)

- **Langizo**: Yankhani funso **limodzi** lokha mwa mafunso **awiri** ali m'munsiwa.Sankhani mutu wa chimangirizo kapena kalata. Mawu a chimangiriozo chanu kapena kalata yanu asachepere **100** koma asabzole **150**

1. Lembani chimangirizo pa mutu wakuti ' Nkhanza kwa ana". Mwa zina tsatani izi polemba chimangirizo chanu.

   **Ndime yoyamba**
   - Nkhanza zomwe ana amakumana nazo
   - Mzanu yemwe anachitilidwa nkhanza
   - Malo amene nkhanza zidachitikira

   **Ndime yachiwiri**
   - Njira zopewera nkhanza
   - Komwe mungakanene patachitika nkhanza
   - Mabungwe omwe amathana ndi nkhanza

   **Ndime yachitatu**
   - Kufunikira kwa kuphunzitsa ana zokhudza nkhanza
   - Kuipa kwa nkhanza

**KAPENA**

2. Yerekezani kuti mwasankhidwa kuti mukayambe folumo 1 kusukuku yogonera komweko ya anyamata ndi atsikana omwe ndipo mukusoweka fizi. Lembani kalata kwa phungu wa m'dera lanu yomupempha thandizo. Mwa zina tsatani izi polemba kalata yanu.

   **Ndime yoyamba**
   - Dzina lanu
   - Komwe munkaphunzira
   - Komwe akusankhirani

   **Ndime yachiwiri**
   - Thandizo lomwe mukufuna
   - Chifukwa chomwe mukupempha thandizoli

   **Ndime yachitatu**
   - Zomwe mudzachite thandizolo likadzapezeka

______________________________________________

______________________________________________

______________________________________________

______________________________________________

______________________________________________

______________________________________________

______________________________________________

## GAWO B (MALIKISI 20)
## KUMVETSA NKHANI

3. Werengani nkhani yotsatirayi mosamala kwambiri kenaka yankhani mafunso otsatirawo.

### ANA A SUKULU

Anyamata ndi atsikana amapita kusukulu kukaphunzira zinthu zambiri monga ukhondo, khalidwe labwino ndi kutsatira malamulo.

Ukhondo amaphunzira kuti azilewa matenda ndi kukhala ndi moyo wathanzi. Uve umadzetsa tizilombo toyambitsa matenda omwe munthu akhoza kufa nawo.

Ana amaphunziranso za makhalidwe abwino. Izi zawathandiza kulemekeza makolo awo ndi anthu ena akuku.

Kusukulu ana amaphunzira mosiyanasiyana. Ana ena amalimbikira sukulu koma ena amachita ulesi. Ana a ulesi kawirikawiri amalephera mayeso pomwe olimbikira komanso a changu amakhoza mayeso.

Chinthu chomwe mwana wasukulu aliyense ayenera kudziwa ndi chakuti kusukulu kulibe kalopo kapena mfulu. Kawirikawiri kusukulu kumapezeka anyamata ena kapena atsikana ena omwe amavutitsa anzawo achilendo. Kusukulu kumene kuli aphunzitsi odziwa udindo wawo, ana ozunza anzawowa amalangidwa. Kuzunza munthu opanda chifukwa ndi khalidwe laupandu. Koma kukoma mtima ndi chinthu chofunika kwambiri popeza kumaonetsa kusiyana pakati pa anthu ndi nyama.

Mwana wasukulu sayenera kukwatiwa kapena kukwatira. Ili ndi limodzi mwa malamulo apasukulu. Malamulo amatchinjiriza ophunzira ngakhale ophunzirawo amaganiza kuti malamulo amachepetsa ufulu wawo. Aphunzitsi ayenera kufotokozera ophunzirawo ubwino wotsatira malamulo popewa kuti patsogolo angadzanong'oneze bondo.

**Tsopano yankhani mafunso otsatirawa pa mizere ili pa funso lililonse**

a. Perekani zinthu ziwiri zomwe anyamata ndi atsikana amakaphunzira kusukulu
_______________________________________________
_______________________________________________ 2malikisi

b. Kodi ukhondo ndi wofunika bwanji kwa ophunzira?
_______________________________________________
_______________________________________________ 1malikisi

c. Tizilombo toyambitsa matenda timabwera bwanji?
_______________________________________________
_______________________________________________ 1malikisi

d. N'chifukwa chiyani ana ena amalephera mayeso?
_______________________________________________
_______________________________________________ 2malikisi

e. Lembani khalidwe loipa lomwe ophunzira ena amakhala nalo kusukulu
_______________________________________________
_______________________________________________ 2malikisi

f. Perekani mawu ofanana m'matanthauzo ndi awa:
   i. Uve ______________________________ malikisi 1
   ii. Achilendo ______________________________ malikisi 1
   iii. Kutchinjiriza ______________________________ malikisi 1

g. Ndi aphunzitsi otani omwe amapereka chilango kwa ana akhalidwe loipa?

______________________________________________________________________

______________________________________________________________2malikisi

h. Kodi kukoma mtima n'kofunika bwanji?

______________________________________________________________________

______________________________________________________________2malikisi

i. Perekani tanthauzo la chining'a ichi " angadzanong'oneze bondo"

______________________________________________________________________

______________________________________________________________2malikisi

j. Lembani udindo uwiri wa aphunzitsi

______________________________________________________________________

______________________________________________________________2malikisi

k. N'chifukwa chiyani ophunzira amadana ndi malamulo apasukulu?

______________________________________________________________________

______________________________________________________________2malikisi

## GAWO C (MALIKISI 10)

Yankhani mafunso onse awiri m'gawoli

4. (a) Werengani kankhanika ndipo muyankhe mafunso otsatirawo.

"Pepani anthu nonse mwafika pano. Tsopano ndi nthawi yoti tiyambe mwambo woperekeza mfumu yathu yogona apayi."

**Mafunso**

i. Kodi malonjewa angaperekedwe pa mwambo wanji?
____________________________________________________________malikisi 1

ii. Lembani udindo wa munthu amene angapereke malonjewa.
____________________________________________________________malikisi 1

iii. Kodi mawu oti "mfumu" akutanthauzanji?
____________________________________________________________malikisi 1

(b) Perekani njira ziwiri zomwe tingasamalire odwala chifuwa chachikulu.

______________________________________________________________________

______________________________________________________________malikisi 2

## KUPANGA ZIGANIZO

**5. Pangani ziganizo zomveka bwino ndi mawu awa:**

a. mkoko

______________________________________________________________________

b. olusa

______________________________________________________________________

c. mwachangu

______________________________________________________________________

d. tsinakhutu

______________________________________________________________________

e. mbee

______________________________________________________________________

## GAWO D (MALIKISI 40)

- Zungulizani lembo lokhoza (A, B , C kapena D) m'mafunso otsatirawa

**Mafunso 6 mpaka 10: Sankhani mitundu ya mawu omwe atsekedwa mzere kunsi kwawo mziganizo zotsatirazi**

6. Mwana wadwala kwambiri
   A. Dzina C. Muonjezi
   B. Mneni D. Mfotokozi
7. Hehede! Ndapambana mayeso.
   A. Mvekero C. Mfotokozi
   B. Mfuwu D. Mneni
8. Kondwani watenga zake.
   A. Mlumikizi C. Mfotokozi
   B. Mneni D. Mlowammalo
9. Khalidwe limeneli walitenga kuti?
   A. Dzina C. Mlowammalo
   B. Muonjezi D. Mkuluwiko
10. Usadutse pano palibe njira.
   A. Dzina C. Mneni
   B. Mfotokozi D. Muonjezi

**Mafunso 11mpaka 15: Sankhani gulu la mayina omwe atsekedwa nzere kunsi kwawo m'ziganizo zotsatirazi**

11. Makapu aja asweka
   A. Chi – Zi C. Li –Ma
   B. U – Ma D. Mu – Mu
12. Kudula mitengo mwachisawawa ndi koipa.
   A. U – Ma C. Mu – Mi
   B. Ka – Ti D. Chi – Zi
13. Kulima nkopindulitsa masiku ano.
   A. Ku – pa – mu
   B. KU + tsinde la mneni
   C. U – Ma
   D. Ka – Ti
14. Iwo amalima nyemba.
   A. Chi – Zi C. I – Zi
   B. U – Ma D. Mu – Mi
15. Nkhwangwa yagwera m'madzi
   A. Mu – Mi
   B. Mu –A
   C. LI –Ma
   D. Ku –pa – mu

**Mafunso 16 mpaka 20: Sankhani chachikazi cha mayina awa:**

16. Nkhunzi
   A. Mnzambwe C. Mtheno
   B. Mthoni D. Mfule
17. Chipsolopsolo
   A. Tambala C. Thanzi
   B. Msoti D. Nkhuku
18. Mphulu
   A. Mfule C. Tonde
   B. Nkhosa D. Mzidzi
19. Tonde
   A. Mkota C. Tonde
   B. Mbuzi D. Thadzi
20. Gocho
   A. Boyi C. Muphwa
   B. Muna D. Chumba

**Mafunso 21 mpaka 25: Sankhani mitundu ya nthambi zomwe zatsekedwa mzere kunsi kwawo mziganizo zotsatirazi**

21. Ana akusewera apowo ndi akwathu
   A. Yoima payokha
   B. Ya dzina
   C. Ya mfotokozi
   D. Ya muonjezi
22. Udzapambana pokhapokha ukadzalimbikira
   A. Ya dzina
   B. Ya muonjezi
   C. Yoyima payokha
   D. Ya mfotokozi
23. Zoti nyanja yathu ikuphwa ndi zoona
   A. Ya muonjezi
   B. Yoyima payokha
   C. Ya mfotokozi
   D. Ya dzina
24. Buku lomwe labedwa ndi langa
   A. Ya dzina
   B. Ya muonjezi
   C. Ya mfotokozi
   D. Yoyima payokha
25. Sindikudziwa chomwe wabwerera
   A. Ya dzina
   B. Yoyima payokha
   C. Yosaima payokha
   D. Ya mfotokozi

**Mafunso 26 mpaka 30: Sankhani mitundu ya misintho ya aneni omwe atsekedwa mzere kunsi kwawo mziganizo zotsatirazi**

26. Iwo amabwerabwera kunyumba
   A. Wochitirana
   B. Wobwerezabwereza
   C. Wotsutsana
   D. Wom'chitira

27. Mtsikana wamwano <u>wamenywa</u>
    A. Wotsutsana
    B. Wochitirana
    C. Wonyadzitsa
    D. Wom'chitira
28. Phungu <u>wamangira</u> nyumba anthu ovutika
    A. Wom'chitira
    B. Wonyadzitsa
    C. Wochitirana
    D. Wochititsitsa
29. Ana <u>agwetsana</u> panjinga
    A. Wotsutsa
    B. Wochitidwa
    C. Wochititsa
    D. Wochitirana
30. Iwo <u>amatula</u> pepala pakhomo
    A. Wochitirana
    B. Wom'chitira
    C. Wotsutsa
    D. Wochitidwa

**Mafunso 31 mpaka 35: Sankhani mitundu ya nthawi za aneni yomwe yatsekeda mzere kunsi kwawo**

31. Iwo <u>adalima</u> chimanga
    A. Yakale
    B. Yamtsogolo
    C. Ya kawirikawiri
    D. Yopitilira yamtsogolo
32. Atsikana <u>akuvina</u> chiterera ya mtsogolo
    A. Ya mtsogolo
    B. Yopitirira
    C. Yatsopano yopitirira
    D. Yamtsogolo yopitilira
33. Ife <u>tidzalemba</u> mayeso
    A. Yatsopano
    B. Yakawirikawiri
    C. Yakale
    D. Yamtsogolo
34. Ife <u>timasamalira</u> chilengedwe.
    A. Yatsopano
    B. Yakale
    C. Yakale yopilitira
    D. Yakawirikawiri
35. Mvula <u>yagwa</u> kwambiri
    A. Yakawirikawiri
    B. Yobwereza
    C. Yakale
    D. Yatsopano yathayi

**Mafunso 36 mpaka 40: Sankhani mawu otsutsana mmatanthauzo ndi omwe atsekedwa mzere kunsi kwawo**

36. Inu ndi ana <u>aulesi.</u>
    A. Olimbikira C. Achidwi
    B. Amasewera D. Ankhanza
37. Ife tasamba madzi <u>otentha</u>
    A. Owotcha C. Owira
    B. Ajuu D. Ozizira
38. Iye wabwetsa <u>zopewerera</u>
    A. Zakale C. Zochukula
    B. Zokwanira D. Zamakono
39. Anyamata <u>amanga</u> mpanda.
    A. Akonza C. Apasaka
    B. Akhulula D. Amasula
40. Atate <u>adavala</u> malaya okongola
    A. Adachotsa C. Adayanika
    B. Adavula D. Adayalula

**Mafunso 41 mpaka 45: Sankhani matanthauzo a mikuluwiko yotsatirayi**

41. Nkhondo ndi anansi
    A. Abale amatikonda pamatendere pokha
    B. Abale nthawi zina amafunirana zoipa
    C. Abale nthawi zina sayamika
    D. Abale sawoneka pamavuto
42. Ndionetsetse adathetsa nkhosa
    A. Kuzengereza kumapezetsa mavuto
    B. Changu chimapezetsa mavuto
    C. Ukaona zinthu udziuza anzako
    D. Tidzionetsetsa zinthu tisanachitepo kanthu
43. Pakadafunda padajiwitsa galu
    A. Kukonda kukhala malo amodzi
    B. Sibwino kukhalitsa pamalo
    C. Kukomedwa pochita zinthu kumabweretsa mavuto
    D. Sibwino kupanga zinthu mwaulesi
44. Mphungu sataya nthenga
    A. Munthu wadyera
    B. Munthu odzikonda
    C. Munthu omana
    D. Munthu wabodza
45. Madzi akatayika sawoleka
    A. Ndikovuta kuwolera madzi akatayika
    B. Zinthu zina zikalakwika zizingakonzekenso
    C. Zinthu zikasowa sizingapezeke
    D. Kutaya mwayi wopezapeza

**MAFUNSO ATHERA PANO**

**NB: Onetsetsani kuti pepalali lili ndi masamba asanu ndi awiri**